

Mphamvu ku Anthu:

Ndondomeko ya Kalondolondo wa Kagwiritsidwe
Ntchito ka ndalama za Maboma Ang'onoang'ono



Dr. Asiyati Chiweza



USAID
FROM THE AMERICAN PEOPLE



National Democratic Institute ndi bungwe lothandiza mwachifundo, losayimira chipani chilichonse komanso silaboma, limene limakhudzidwa ndi zikhumbokhumbo za anthu padziko lonse lapansi kuti akhale muufulu ndi kulimbikitsidwa pa nkhani ya ufulu wachibadwidwe.

Kuyambira pamene linakhadzikitsidwa mu chaka cha 1983, bungweli pamodzi ndi mabungwe ena a m'dziko muno akugwira ntchito yolimbikitsa ufulu polimbikitsa zipani, mabungwe a boma ndi nyumba yamalamulo, pakutetezela zisankho ndi kulimbikitsa anthu kutenga nawo gawo, kusasunga zinsinsi ndi kukhulupirika pa nkhani ya za chuma m'boma.

Anthu ogwira ntchito m'bungweli ndi anthu ogwira ntchito modzipereka pa nkhani za ndale ochokera m'mayiko oposera 100, amasonkhanitsa anthu ndi magulu osiyanasiyana kugawana maganizo, nzeru ndi upangiri. Anthuwa amaphunzira zambiri zokhudzana ndi chitukuko cha ndale pa dziko lonse lapansi zimene angatengele ku mayiko awo. Njira imeneyi imathandizila kupititsa patali uthenga woti ngakhale palibe njira imodzi yoyendetsela ndale, pali njira zina zoti anthu a ndale atha kugawana.

Ntchito ya bungweli imathandizira maulamuliro amene anakhadzikitsidwa padziko lonse lapansi okhudzana ndi ufulu wachibadwidwe. Imapititsanso patsogolo maubale ovomerezeka pakati pa anthu, mabungwe a za ndale ndi anthu amene anasankhidwa kugwira ntchito, ndikulimbikitsa luso lawo lopititsa patsogolo umoyo wa bwino wa anthu. Ngati mukufuna kudziwa zambiri za bungweli, onani pa www.ndi.org.

Copyright © National Democratic Institute for International Affairs (NDI) 2015. Magawo ena a zomwe zalembedwa mu ndondomekoyi zitha kuzalembedwanso kapena kutanthauziridwa pakugwiritsidwa ntchito munjira zina zosafuna ndalama. Bungwe la NDI ndilimene lavomerezeka ngati mwini wa ndondomekoyi.

455 Massachusetts Avenue, NW, Floor 8
Washington, DC 20001
Telephone: 202- 728-5500
Website: www.ndi.org

Ndondomekoyi inatheka ndi thandizo lochokera ku DFID ndi USAID. Maganizo onse alembedwa mundondomekoyi ndi a anthu amene anayilemba osati a DFID kapena USAID.

Kuthokoza

NDI ikuthokoza ogwira ntchito ndi onse amene anatenga nawo gawo ndi kuyikapo nzeru zawo polemba ndondomekoyi: Greg Brown, Governance Senior Program Assistant; Henry Chilobwe, NDI Malawi Program Officer, Dr. Asyati Chiweza, Katswiri wa ntchito za maboma ang'ono; Kiswell Dakamau, Mkulu woyendetsa ntchito za maboma ang'ono ku Unduna wa Zamaboma Ang'ono ndi Chitukuko cha M'midzi and Rural Development; Paul Friesen, SEA Program Assistant; Laura Hinkle; SEA Program Assistant, Dalitso Kubalasa, Mkulu wa bungwe la Malawi Economic Justice Network; Pamela Kuwali, NDI Malawi Senior Program Manager; Sandy Quimbaya, Mkulu wa bungwe la NDI ku Malawi; Farha Tahir, SEA Senior Program Officer; Patricia Nyirenda, Economist wa ku National Local Government Finance Committee and Wendy Singh, SEA Senior Program Manager.

Bungwe la NDI likuthokoza mwapadera thandizo limene linapelekedwa kuchokera ku DFID ndi USAID pamene limalemba ndondomekoyi.

Za mkatimu

KUTHOKOZA	2
1.0 MAU OYAMBA.....	5
1.1 MAU ACHIDULE AWA AKUYIMILA IZI	5
1.2 ZINAYAMBA BWANJI	6
1.3 UBWINO WA KALONDOLONDO WAKAGWIRITSIDWE KA CHUMA M'MABOMA ANG'ONO	6
2.0. KODI KABUKUKA NDI KA NDANI?	7
3.0. NTCHITO NDI UDINDO WA MAKHONSOLO A M'MABOMA ANG'ONO M'MALAWI	8
3.1 MFUNDO ZOMWE MABOMA ANG'ONO AMATSATA M'MALAWI.....	9
4.0 UBWINO WA KALONDOLONDO WAKAGWIRITSIDWE KA CHUMA CHA MA BOMA ANG'ONOAG'ONO	11
5.0 KOMWE KUMACHOKERA NDALAMA ZA M'MABOMA ANG'ONO	11
5.1 NDALAMA ZOCHOKERA KULIKULU LA BOMA.....	11
5.2 NDALAMA ZOMWE MABOMA ANG'ONO AMAPEZA PAIWO WOKHA.....	13
5.3 THUMBA LANDALAMA ZACHITUKUKO CHA M'MABOMA ANG'ONO	13
5.4 NDALAMA ZA ANTHU ACHIFUNDO NDI MABUNGWE OSAKHALA ABOMA	13
6.0 NJIRA ZOYENERA KUTSATA POPANGA KALONDOLONDO WA CHUMA CHA BOMA.....	13
7.0 ZINTHU ZOMWE ZINGAPANGITSE KUTI KALONDOLONDO WA NDALAMA ZAM'MABOMA ANG'ONO AYENDE BWINO NDI:	26
KWINA KOMWE MUNGATHE KUPITILIZA KUWERENGA ZA MALANGIZO NDI UKU.....	26

Mau achidule awa akuyimira izi

ADC:	Area Development Committee
AIP:	Annual Investment Plan
CBOs:	Community Based Organizations
CDF:	Constituency Development Fund
CSOs:	Civil Society Organization
DC:	District Commissioner
DDP:	District Development Plan
DESP:	District Education Sector Plan
DHO:	District Health Office
DOF:	Director of Finance and Administration
DPD:	Director of Planning and Development
DDP:	District Development Plan
DIP:	District Development Plan
FBOs:	Faith-Based Organizations
GRF:	General Resource Fund
GoM:	Government of Malawi
IDF:	Infrastructure Development Fund
LDF:	Local Development Fund
LDP:	Local Development Plans
MDAs:	Ministries, Departments and Agencies
MGDS II:	Malawi Growth and Development Strategy II
MP:	Member of Parliament
NDI:	National Democratic Institute for International Affairs
NGO:	Non-Governmental Organization
NLGFC:	National Local Government Finance Committee
ORT:	Other Recurrent Transactions
PET:	Public Expenditure Tracking
PETS:	Public Expenditure Tracking Surveys
VAP:	Village Action Plans
VDC:	Village Development Committee

1.0 Mau Oyamba

Cholinga cha kauniuni wa kayendetsedwe ka ndalama za boma ameneyu ndi kuthandiza ma khansala ndi ogwira ntchito ena apa khonsolo kuchita kalondolondo pa ndondomeko ya zachuma yapa khonsolo. Ndongomeko imeneyi ikuthandizira pa mfundo zounikanso kagwiridwe ka ntchito za boma pa ma gawo a kupereka mphamvu ku anthu ndi kagwiritsidwe ntchito ka chuma cha boma. Kudzera mu ndondomeko imeneyi, ma khansala ndi ena ogwira ntchito pa khonsolo azitha kudziwa ngati ndalama za pa khonsolo zikugwira ntchito moyenera molingana ndi mfundo zomwe zinayikidwa pa ndondomeko. Kauniuni ameneyu ali ndi kuthekera kothetsa katangale ndi kusokonekera kwa ndalama pa khonsolo, komanso kuthandizira kukweza miyoyo ya anthu mmadera omwe makhonsolo amatumikira pakulimbikitsa kugwira ntchito moonekera ndi mokhulupirika.

Kalondolondo ameneyu ali ndi njira zingapo zomwe ma khonsolo angaunikire ndondomeko yawo ya zachuma komanso ndi chipangizo chomwe chimagwiritsidwa ntchito mmaiko ambiri pa dziko lapansi pochepetsa kuonongeka kwa chuma pa zinthu zosayenera komanso kuonetsetsa kuti ntchito zikugwiridwa moonekera. Kalondolondo ameneyu akutsindikanso za ntchito ya kuyang'anira yomwe ma khansala amakhala nayo. Ndongomeko'yi ndiyosalekeza, ndipo imathandiza kubweretsa boma ku anthu kuphatikizira kuwapatsa mphawu anthu pakulimbikitsa ndikubweretsa pafupi njira zomwe iwo angatengerepo gawo popeza yankho la mabvuto am'madera mwao.

Kuti ndondomeko'yi igwire bwino ntchito, ndipofunika kugwirana manja pakati pa ma gawo onse kuyambira ama bungwe, makhansala, adindo apa boma, aphungu ndi ogwira ntchito mdera, kuti azikhala ndi chiganizo ndi cholinga chimodzi ndi kudzipereka pa kagwiridwe kantchito.

A Unduna wa Maboma Aang'ono ndi Chitukuko cha M'midzi molumikizana ndi nthambi yoona zachuma cha maboma aang'ono akuthokoza ndi kuyamikira thandizo lochokera kubungwe la chitukuko cha maiko la ku America la United States Agency for International Development (USAID) ndi nthambi ya chitukuko cha maiko ya boma la Britain la Department for International Development (DfID) kudzera mu bungwe lolimbikitsa demokalase ndi ufulu la National Democratic Institute (NDI).

1.1 Zinayamba bwanji

Dziko la Malawi likukhadzimitsa ndondomeko yopititsa patsogolo zitukuko m'dzikoli (MGDS II) ngati njira yothandiza kubweretsa chuma chopititsira patsogolo nkhani ya za chuma komanso chitukuko zomwe zingachepetse umphawi.

Njira yayikulu yokhazikitsira ndondomekoyi (MGDS II) ndi ndondomeko yakagwiritsidwe ka chuma cha boma. Magawidwe a chuma cha boma mu ndondomeko yakagwiritsidwe ka chuma cha boma amapangidwa ndi m'mene ayikidwira mu ndondomeko yopititsa patsogolo zitukuko m'dzikoli (MDGS). Koteru ndizofunika kuonetsetsa kuti chuma chimene chili mu ndondomeko yakagwiritsidwe ka chuma cha boma chapititsidwa komwe chikuyenera kukagwira ntchito yake yoyenera potsatira m'mene chinayikidwira mundondomeko yopititsira patsogolo dzikoli.

Kalondolondo wa kagwiritsidwe ka chuma ndikofunikira powona kalowedwe ndi kagwiritsidwe ka chuma cha boma kuchokera komwe zachokera kupita kwa anthu oyenerera ndi njira yothandiza mabungwe kukhala okhulupirika pa kagwiritsidwe ka chuma komanso kuona kuti chuma chomwe chaperekedwa chafikiradi anthu oyenerera munthawi yake ndi kugwiritsidwa ntchito yake moyenerera.

Pali njira zambiri zimene zimagwiritsidwa ntchito popanga kalondolondo wa chuma cha boma. Njira zina zodziwika ndi izi: kauniuni wa chuma cha boma, kuonetsetsa za kagawidwe ka chuma cha boma pogwiritsa ntchito mabungwe komanso anthu. Mu chaka cha 2008, likulu la boma la Malawi linayambitsa kafukufuku wa kalondolondo wa chuma cha boma. Kafukufukuyu amakhudzana ndi kufunsa mafunso anthu omwe adagawiridwa chuma mu ndondomeko ya kagwiritsidwe ka chuma cha boma, izi ndizofunikira chifukwa anthuwa amapereka umboni wa m'mene chuma chagwiritsidwa ntchito komanso m'mene nthito yake yayendera. Ngakhale zili chomwechi, kafukufukuyu amatenga nthawi ndiposo amafuna ndalama zambiri.

1.2 Ubwino wa Kalondolondo Wakagwiritsidwe Ka Chuma M'maboma ang'ono

Ku maboma ang'ono, udindo onse oyang'anira za chuma uli m'manja mwa khonsolo. Ngati ovota, ma khansala a m'madera ndi ofunikira kwambiri kumbali imeneyi. Kalondolondo wakagwiritsidwe ntchito ka chuma ndi njira imodzi yopezera umboni weniweni womwe ungathandize ma khansala, mzika, ndi ena okhudzidwa kuti apeze, amvetsetse, ndi kukambirana za momwe ndalama zingayendetsedwere kuchokera kwa opereka kufikira kwa oyenera kulandira, ndiponso momwe ndalama zikugwiritsidwira ntchito kuonjezerapo kudziwa ngati ndalamazo zikugwiritsidwa ntchito molingana ndi momwe zofunikira ndi zosowa zawo ziliri. Kalondolondo wakagwiritsidwe ka chuma cha m'maboma ang'ono wochitidwa ndi mzika zadziko ndi mafumu ndiwothandiza kwambiri pa nkhani ya Mphamvu ku Anthu yomwe dziko la Malawi likukweza. Mphamvu ku anthu zimapereka mphamvu kwa mzika za dziko komanso mafumu kuti athe kufotokoza zosowa za pamoyo wawo komanso athe kufotokoza za zitukuko zomwe iwo akufuna kwa owayimirira komanso ogwira ntchito ku khonsolo. Njira iyi imapereka mwayi kwa mzika kuti maganizo awo amveke pankhani ya kagwiritsidwe ntchito ka chuma cha boma. Zimakhudzanso ndi Mzika, ma Khansala, mabungwe a m'midzi (CBOs), Mabungwe a mipingo (FBOs), Mabugwe am'madera (ADC) ndi mabungwe a m'midzi (VDC) omwe ndi mamembala komanso mafumu kutenga nawo mbali kulondoloza momwe ndalama za boma zafikira komanso momwe azipezera ndikuzigwiritsira ntchito.

Boma limalimbikitsa kukhulupirika m'boma pogwiritsa ntchito njira zosiyanasiyana, malamulo ndi ndondomeko zingapo. Ngakhale zili chomwechi, pali mavuto ambiri amene amakhalapo omwe amafowoketsa njirazi; komabe, kalondolondo wa kagwiritsidwe kachuma cha boma anapangidwa kuti azionetsetsa kagawidwe ka chuma, kugwiritsidwa ntchito kwake ndi zitukuko za boma. Njira ya kalondolondo wa kagwiritsidwe ka chuma ndiyofunika kwambiri kufotokozeledwa kwa ena onse ngati njira yothandiza kwambiri osati njira yongoonera m'mene chuma chayendera basi (NDI, 2013). Ndizofunikanso kuwatsimikizira ogwira ntchito m'maboma ang'onoang'ono ndi ena onse oyimilira kuti cholinga cha njira imeneyi ndikupititsa patsogolo

chitukuko m'maboma ang'onoang'ono ndikulimbikitsa ubale pakati pa anthu ndi owagwirira ntchito zachitukuko. Pakuonetsetsa m'mene chuma chagwiritsidwira ntchito, makhansala ndi ena ogwira ntchito zachitukuko, mabungwe a boma ndi anthu onse atha kupititsa patsogolo zofuna zaboma kuonetsetsa kuti chuma cha boma chikugwiritsidwa ntchito moyenerera. Anthu ndi mabungwe akabwera pamodzi ndikugwira ntchito limodzi, zotsatira zake zitha kukhala njira yabwino ya kayendetsedwe ka boma, kugwira ntchito bwino ndi zotsatira zabwino zachitukuko komanso kupititsa patsogolo maganizo abwino a anthu pakayendetsedwe ka boma (NDI 2010). Cholinga ndi chakuti pamene vuto lawonedwa kapena zofowoka zazindikidwa, boma liri ndi mwayi owona zofowokazo.

2.0. KODI KABUKUKA NDI KA NDANI?

Kabukuka kalembedwa munjira yoti kapereke ndondomeko kwa maboma ang'onoang'ono M'malawi kuti awone m'mene angalondolere ndondomeko ya kagwiritsidwe ka chuma cha maboma ang'onong'ono ku maofesi a boma komanso makomiti a ntchito za boma. Buku la makhansala ndi anthu ena ogwira ntchito ku maofesi a boma lomwe linasindikizidwa mchaka cha 2014 limati: ma ofesi a chitukuko a boma ali ndi ntchito yofunikira yoonetsetsa kuti chuma cha boma chikuyendetsedwa moyenera. Zina zofunikira zomwe makhansala ndi anthu ena ogwira ntchito zachitukuko akuyenera kuchita pogwira ntchito imeneyi ndi izi:

- Kuvomereza ndondomeko ya chuma cha chitukuko;
- Kuonetsetsa kuti maofesi a chitukuko akutha kupereka ndondomeko ya m'mene agwiritsira chuma cha boma mu nthawi yake;
- Kuonetsetsa bwinobwino ndondomeko zonse za m'mene chuma chagwiritsidwira ntchito komaso kuwunikira ogwira ntchito ku ofesi ya chitukuko zakagwiritsidwe ka chuma cha boma;
- Kuwaziwitsa a komiti ya maboma ang'onoang'ono m'dziko lonse la Malawi (National Local Governance Committee) ngati pali maganizo ena alionse oti chuma cha boma sichinayendetsedwe bwino kapena kubedwa kuti akomiti afufuze;
- Kuonetsetsa kuti malamulo awa: Lamulo la kagwiritsidwe ka chuma cha boma (2003), Lamulo lakugula katundu ogwiritsidwa ndi boma (2003), Lamulo la kauniuni wakagwiritsidwe ka ndalama (2003) ndi Lamulo la zachinyengo (1998) ndi Malamulo ena onse a boma akutsatidwa nthawi zonse;
- Kuonetsetsa kuti chuma chilichonse chopita ku ofesi ya chitukuko chalengezedwa pogwiritsa ntchito mawayilesi kapenanso kukhoma m'mabolodi, m'mitengo ndi njira zina;
- Kugwirizana ndi likulu la boma, anthu akufuna kwabwino komanso mabungwe akuluakulu a zachitukuko omwe akutumiza chuma kumadera kuti azilengezetsa kuchuluka kwa chumacho mumanyuzipepala, pa wayilesi ndi pa intaneti (kompyuta)

Kalondolondo wa ndondomeko yakagwiritsidwe ka chuma cha boma mu maofesi a boma ndiofunikira ku ntchito za makhansala poyendetsa chuma cha chitukuko. Izi zitha kupangidwa ndi komiti ya za chuma cha chitukuko, anthu kapena magulu amakhansala omwe akuyang'anira ma komiti a ntchito zosiyasiyana zachitukuko. Makhansala awona phindu la njirayi komanso kusavuta kwake poyigwiritsa ntchito pantchito zawo.

3.0 Ntchito ndi Udindo wa makhonsolo a M'maboma ang'ono M'malawi

Kuti kalondolondo wazachuma ayende bwino ndi kofunika kuti ma Khansala adziwe bwino ntchito yawo ndi momwe Khonsolo yawo iyenera kugwirira ntchito, momwe imagwirira ntchito komanso momwe dongosolo lakayendetsedwe kandalama koyenera kamakhalira. Maboma ang'ono M'malawi ndiofunikira kwambiri pokweza chitukuko chamaboma ang'ono komaso kuonetsetsa kuti anthu ali ndi zosowa zawo za pamoyo wa tsiku ndi tsiku maka pa zinthu zomwe zili m'manja mwa maboma ang'ono. Lamulo lopereka Mphavu ku anthu ndi Malamulo am'maboma ang'ono (Local Government

Act, CaP 22:01) limapereka chitsanzo cha ntchito zimenezi ndiponso magawo atatu ndiponso ma komiti apa khonsolo omwe ayenera kuchita zimenezi.

Tebulo I: Chitsanzo cha ntchito za pa khonsolo

Gawo	Zomwe ayenera kupereka	Komiti Yokwaniritsa
Maphunziro	Maphunziro aku pulayimale	Komiti Yamaphunziro
Zaumoyo ndi Kapezedwe kamankhwala	Zipatala zazing'ono, zipatala za amayi oyembekezera, kupewa matenda opatsirana, maphunziro azaumoyo, kusamalira zachilengedwe ndi ukhondo	Zaumoyo ndi Chilengedwe
Zaulimi ndi ulimi wothilira	maphunziro a malimidwe ndi kusamalira ziweto, kupewa matenda a ziweto, kusamalira nthaka, zakudya zoyenera, kukumba ndi kusamalira mayiwe (madamu) aang'ono.	Azaulimi

zachokera m'bukhu la: Decentralisation Policy (1998).

Chonde tsatirani malamulo akagawidwe ka mphavu kuti mudziwe momwe maboma aang'ono akuyendetsera ntchito zawo. Momwe maboma ang'ono amayendera M'malawi amatsata magawo awiri: gawo la ndale, mafumu, ndi anthu asanu oyimirira zofuna zina. Ma khonsolo ali ndi mphavu ndi udindo omwe anapatsidwa kuchokera pa malamulo a dziko la Malawi kuti azitha kupanga chiganizo pa malamulo a momwe maboma ang'ono angadzilamulire komaso angapangire chitukuko m'malo mwa mzika za maboma ang'ono a mdera, kuyanjanitsa ndi kukweza mabugwe oyang'anira mafulu ndikugwirana manja; kupititsa patsogolo ntchito zomangamanga, kukweza ntchito za zachuma ndi kubweretsa chitukuko kwa anthu amudera mwao; kukweza njira zopezera chuma; kutenga gawo poyang'anira dera; ndikupanga malamulo okhudza dera lawo.

Khonsolo imayendetsedwa ndi ma komiti osankhidwa. Izi zikutanthauza kuti asanapange kalikonse a khonsolo, komiti imakumana ndikuvomereza komanso kupereka maganizo ndi uphungu kwa khonsolo yonse kuti ikambirane ndikutsimikiza zokambiranazo. Makomiti osankhidwawa ndiofunika kwambiri chifukwa ndi komwe akhansala a dera amagwira ntchito ndikulimbikitsa zolinga zokhudzana ndi mdera lomwe amayimirira.

Likulu la khonsolo limakhazikitsidwa ndi anthu osankhidwa ndi anthu ena olembedwa ndi khosolo. Limatsogozedwa ndi bwana nkubwa (DC) wa khonsolo ya boma kapena apampando a mzinda mu makhonsolo a m'matauni ndipo iwo udindo wawo ndikuyan'ganitsitsa kuti zolinga za khonsolo zakwaniritsidwa. A DC kapena mkulu woyendetsa ntchito za khonsolo amagwira ntchito mothandizidwa ndi akulu akulu ena omwe amayang'anira mthambi zapa khonsolo. Akulu akulu amenewa ali ndi udindo onunikira khonsolo ndi ma komiti osankhidwa pamomwe angayendetsere malamulo, komanso kuonetsetsa kuti zolinga za khonsolo zakwaniritsidwa. Ogwira ntchito pa khonsolo ndiofunika pa khani ya kayendetsedwe ka zachuma chifukwa iwo ndi omwe amasunga

ZOFUNIKA KUDZIWA:



Ndizofunikira kuti ma khansala adzidziwa udindo wa komiti yosankhidwa komanso udindo wa khonsolo. Dziwani kuti ogwira ntchito pa khonsolo ndi anthu ofunika pa nkhani ya kayendetsedwe kabwino ka chuma chifukwa iwo ndi omwe amasunga zinsinsi ngati bajeti ya khonsolo, masomphenya a boma, ndondomeko zamomwe boma likwaniritsire masomphenya ake ndi ma lipoti ena.

zofunikira pantchito ngati bajeti ya khonsolo, mabungwe omwe akupereka chithandizo ndi ma ripoti (kuphatikizapo ma lipoti a zachuma). Ma bajeti a khonsolo ndi ma repoti ena amalembedweratu ndi anthuwa asanatumizidwe ku komiti yosankhidwa ndi ku khonsolo yonse.

3.1 Mfundo zomwe maboma ang'ono amatsata M'malawi

Malamulo a dziko la Malawi (1994) ndi malamulo a maboma ang'ono (CAP 22:01) amafuna kuti kayendetsedwe kamaboma ang'ono kazipangidwa mwaumodzi, mosabisa, komaso momasuka. Ndime yachitatu ya malamulo a maboma ang'ono (CAP 22:01) imanena kuti kalozera wakayendetsedwe ka maboma ang'ono m'Malawi kakhale kukweza malamulo adziko komaso kukweza ufulu otenga nawo mbali pankhani zachitukuko, Makhansala ndi ena ogwira ntchito ku khonsolo ayenera kumvetsetsa izi ndikuonetsetsa kuti zikutsatidwa:

- a. Kutenga nawo mbali: kutanthauza kutenga gawo pa zithu zosiyana siyana maka pa nthawi yopanga ziganizo pa nthawi yokonzekera, kugwira ntchito komanso kulondoloza ndondomeko yantchito za khonsolo. Chofunika kwambiri pakutenga nawo gawo ndi kuonetsetsanso kuti a mayi, achinyamata, anthu olumala ndi ena omwe amasalidwa akutha kutenga nawo gawo pa chitukuko komaso kayendetsedwe ka dera lanu.
- b. Kupanga zithu mosabisa: kumafunika zintchito zanu ndi zisankho zanu muchitire poyera ndiponso anthu akhale akudziwa nkhani zanu zonse kuti anthu obwera komanso anthu onse athe kudziwa mosavuta ngati njira zoyenerera zikutsatidwa mogwirizana ndi ntchito yomwe muli nayo pa khonsolo.
- c. Kukhulupirika pa nkhani ya zachuma: kutanthauza udindo wotha kuyankha pa njira zomwe zatsatidwa pa ntchito yomwe mwagwira kupyolera mu mphamvu, chuma ndi katundu yemwe munapatsidwa kuti mugwirire ntchito. Narayan (2002) anatanthauza mau oti kukhulupirika pa zachuma (accountability) ngati mphamvu yolamula anthu ogwira ntchito zaboma kuti apereke umboni kuti ndalama ndi chuma chaboma chagwiritsidwa ntchito moyenera.

Kukhulupirika pa nkhani ya zachuma kulipo ma gulu awiri ku maboma ang'ono aliwonse. Njira yoyamba imatchedwa holizonto (horizontal accountability). Njira imeneyi ndi kuthekera kwa ogwira ntchito m'boma ndi olamulira kuonetsetsa komanso kukhulupirika polongosola mbali zina zaboma. Pa njira imeneyi ya holizonto, ndikuthekera kwa ogwira ntchito pakhosolo mwa iye yekha kuona omwe sakugwira ntchito mosamala. Pamenepa tikutanthauza mkulu la khonsolo yemwe ndi a bwana nkubwa, ndi ena onse ogwira ntchito pa khonsolo ndiomwe ali ndi udindo owonetseka kuti nkhani ya za chuma chaboma ikulongosoka ndipo ntchito ya khonsolo ndi amaudindo onse akugwirira ntchito limodzi mogwirizana komaznsa ntchito za maboma ang'ono zikuyenda bwino, ndalama zikulongosoka ndipo zikugwira ntchito yake. Mbali yaikulu kukhulupirika pankhani ya zachuma ya holizonto imakhudzana kwambiri ndi amaudindo osankhidwa kupereka malipoti komaso kufotokozera zochitika kwa okhudzidwa onse. Polongosola za bajeti pa ntchito yawo yonse, ma khansala ndi mabungwe onse a boma akhoza kuwafunsa ogwira ntchito m'boma kuti alongosole pa khani ya zachuma poonetsetsa kuti katundu waboma akugwira ntchito zoyenerera monga momwe chikonzero chinalili. Mbali inaso ndi yokuti khosolo imayankha ku likulu laboma, kugwira ntchito ndi abale omwe amachokera ku mbali zina za boma mokhudzana ndi nkhani ya za chuma komaso ma lipoti a ma pologalamu, akauniuni okhudza za chuma ndi oyang'anira kagwiridwe ka ntchito.

Njira ina yokhulupirika pa nkhani ya zachuma imatchedwa vetiko, (Vertical Accountability). Iyi imatanthauza kukhulupirika kwa boma kwa mzika zake, kumabugwe omwe siaboma, kwa atolankhani ndiena onse. Izi zikutanthauza kuti anthu osankhidwa ngati ma khansala ndi mamembala a ku Nyumba ya Malamulo ndiokhulupirika pa nkhani ya zachuma kwa anthu omwe adawasankha komanso kuonetsetsa kuti maboma ang'ono akupereka zosowa za anthu panthawi yake moyenera ndiponso kuti ndalama za boma zomwe amapeza amaboma ang'ono zikugwira ntchito yake moyenera. Pachifukwachi anthu osankhidwa ayenera kufotokozera anthu nkhani zokhudzana ndi ma pulojeketi ndi ndondomeko zachitukuko zonse zomwe boma ndi madera akonza komanso mabajeti omwe akonzedwa kulongosola za chitukuko cham'madera, kulondoloza bajeti komanso kutambasula ndikuunika momwe zinthu zikuyendera. Misonkhano yapafupipafupi ndiyofunika kwambiri chifukwa ndi njira inanso yolumikizitsira anthu osankhidwa ndi iwo amene adawasankha.

Pali njira zambiri zopititsira patsogolo kukhulupirika pa nkhani ya zachuma:

- a. Ndikofunikira kwambiri kuti makhonsolo adzidziwa mmene zinthu zikuyendera, kulandira ndikuunika ma bajeti ndi malipoti amomwe ndalama zagwiritsidwira ntchito komanso kuonetsetsa kuti nkhani zonsezi zikuyendetsedwa moganizira chomwe chingathandize mzika za m'dera lawo.
- b. Ma khonsolo atha kukhala ndi mabukhu awo olongosola za zachuma, kupeza umboni weniweni pamaganizo akayendetsedwe ka za chuma komanso kupeza zotsatira ndalama zomwe zaonongeka ndi kupereka izi kwa anthu onse kuti adziwe zomwe zikuchitika.
- c. Maboma ang'ono atha kuonetsetsa mwa iwo wokha kuti onse okhudzidwa ngati mabungwe omwe siaboma atha kupeza bajeti ndi dongosolo lakagwiritsidwe ntchito ka ndalama opanda owakaniza kapena kuletsedwa.
- d. Makhonsolo atha kupereka dongosolo la bajeti kuti anthu onse athe kuona komanso kuipeza ngati ali osangalatsidwa kutero.
- e. Ma khonsolo mogwirizana ndi mabugwe atha kulondoloza momwe mfundo ndi zolinga zachitukuko (policy) zovomerezeka zikukwaniritsidwira ndikuonetsetsa kuti pali mfundo zokhazikika zochepetsera kubedwa ndi kusakaza chuma kuti chitukuko chipite patsogolo.
- f. Maboma ang'ono atha kupititsa patsogolo kufalitsa nkhani kwa anthu onse ndikuika njira kuti zosowa za anthu zipezeke. Mwachitsanzo kukhazikitsa ma komiti omva maganizo a anthu, magulu omwe mzika zingakumane ndi kukambirana ma bajeti a m'maboma momasuka, kutengapo gawo pokonza bajeti ndi njira zina zotero.



NKHANI YAIKULU:

Kalondolondo wakagwiritsidwe ntchito kandalama zaboma ndi njira imodzi yolimbikitsira kuthekera kwa makhansala kuti awonetsetse komaso kukonza holizonto komaso vetiko accountability komaso kuchepetsa zinsinsi pa nkhani ya ndalama m'maboma ang'ono.

4.0 UBWINO WA KALONDOLONDO WAKAGWIRITSIDWE KA CHUMA CHA MA BOMA ANG'ONOANG'ONO

Ntchito yowonetetsa kuti pali kukhulupirika pachuma chaboma imafunika kuti pakhale gulu la anthu osankhidwa kuti awayimilire lomwe lili ndi luso pa ntchito zamanja, komaso zoyanjanitsa anthu kuphatikizapo chikoka pamayankhulidwe. Kalondolondo wakagwiritsidwe ntchito ka chuma ndi njira imodzi yolimbikitsa makhansala kuti akhale ndi luntha poyang'anira kalondolondo wa chuma chaboma kudzera mu njira ya horizonto komanso vetiko komaso kupititsa patsogolo maboma ang'ono kugwira ntchito mopanda zinsinsi. Kalondolondo wakagwiritsidwe ntchito ka chuma cha boma kali ndi ubwino uwu:

- a) Zimathandiza makhansala kulandira ndikuunika bajeti komanso malipoti akagwiritsidwe ntchito ka ndalama ndikuonetsetsa kuti zonse zikutsatira zinthu zomwe zili zothandiza mzika.
- b) Imakhala ngati njira yopezera nkhani komanso kudziwitsira mzika nkhani komanso anthu ena onse okhudzidwa za momwe chuma cha boma chikugwiritsidwira ntchito.
- c) Zimapereka kuthekera kwa anthu okhudzidwa a m'maboma ang'ono kuti athe kukambirana za komwe kukuchokera ndalama ndi momwense ndalama zikugwiritsidwira ntchito.
- d) Njira imeneyi imapereka mwayi wofufuza kuti maganizo osiyanasiyana aperekedwe komanso imabweretsa kuthekera kokambirana zolinga ndi zofuna (policies) ndi zofunika kumaboma ang'ono.
- e) Zimapereka mwayi kwa anthu osankhidwa ndi mzika kugwirira ntchito limodzi poonetsetsa kuti ndalama za khonsolo zikugwiritsidwa ntchito yoyenera ndiponso yolingana ndi ndalamazo.
- f) Ndi njira yopezera umboni pamene ndalama za boma zikuonongedwa poonetsetsa kuti ndalama zikuloweradi komwe zinayenera kupita, komaso ngati zikugwira ntchito yomwe inalonjezedwa.
- g) Imalimbikitsa chikhulupiriro pakati pa mzika zadziko ndi maboma ang'ono.
- h) Zimaonetsetsa kuti ndalama zizipitilira kubwera ku maboma ang'ono ndiponso zikumaperekedwa mokwanira..

5.0 Komwe Kumachokera Ndalama za Maboma Ang'ono

Ndalama za m'maboma ang'ono zimachokera makamaka ku ndalama zomwe maboma ang'onowo amazipeza akalandila misonkho ing'ono ing'ono komaso kuchokera ku likulu la boma ngati thandizo ngati njira yodalilika yomwe imathandiza bajeti yapachaka. Mwanthawi zina anthu achifundo amathanso kuthandiza pa bajeti ya maboma ang'ono. Nthawi zambiri, ndalama za anthu achifundo zimaperekedwa kunjira kwa bajeti kuthandizira ma pulojekiti osankhidwa. Njira zina zopezera ndalama zothandizira ndondomeko ya zantchito zam'maboma ang'ono zili ngati thumba lachitukulo cha m'mudzi komanso mabungwe omwe siaboma (NGOs). Amenewa amathandiza ntchito zina zomwe sizinaikidwe mu bajeti.

Izi ndi zina mwa njira zopezera ndalama zomwe ziyenera kuganiziridwa polondola momwe amaboma ang'ono amayendetsera ndalama zaboma:

5.1 Ndalama zochokera kulikulu la boma

Ndalamazi zimakhala zamalamulo ndi zina zopanda malamulo zochokera ku Unduna woona Zandalama za boma kudzera ku ofesi ya Mlembi wankulu owona zachuma chaboma, (Accountant General) zomwe zimaperekedwa ku buku laku banki la khonsolo. Ndalamazi zimaperekedwa mwezi ndi mwezi ngati pali bajeti yovomerezeka komanso lipoti la ndalama zolowa ndikutuluka.

Ndalama zoperekedwa ndi malamulo ndi ndalama zomwe zimaperekedwa ku nthambi/zigawo

za khonsolo kuti athe kugwiritsa ntchito yomwe auzidwa kuti apange. Pakali pano kuli mthambi zokwana 15 motere: Zaulimi, Zaumoyo, Zamaphunziro, Zachilengedwe, Zamadzi, Zamitengo, Zansomba, Zantchito, Zamalonda, Za ku National Registration Bureau (bungwe lakalemba), Za achinyamata ndi masewera, zajenda, Zamaulendo, Zaulimi othilira, ndi zanyumba. Kuphatikiza ndalama zazigawo, ndalama zina zoperekedwa ndi malamulo ku maboma ang'ono ndi zokhudzana ndi zomangamanga (infrastructure Development Fund), Ndalama zokonzera miseu ya m'mizinda komaso ndalama zakonsitichuwense (Constituency Development Fund).



Ndalama zina ndi zomwe zimaperekedwa mopanda lamulo zimaperekedwa ngati thandizo longoperekedwa (General Resource Fund (GRF)). Ndalamazi zimaperekedwa ngati ndalama zakabwerezabwereza zothandizira kuyendetsa ntchito zatsiku nditsiku m'maboma ang'ono ndi ntchito zina zomwe zingapezeke. Kuphatikiza apo, ma khonsolo amalandila thandizo lopititsira patso ngolo ntchito zachitukuko.

5.2 Ndalama zomwe maboma ang'ono amapeza paiwo wokha

Izi ndi ndalama zomwe amalandira komanso kugwiritsa ntchito amaboma ang'ono kuchokera: Pamisonkho yakatundu, ndalama zochokera ku misika, ndalama zochokera ku misonkho ya malo omwe anthu amagwiritsa ntchito, misonkho ndi ziphaso zina; Ndalama izi ndi zomwe amaboma ang'ono amatha kugwiritsa ntchito zothandizira kutukula khonsolo. Ndikofunika kuti anthu okhala pakhonsolo adzionetsetsa njira zomwe ndalama zomwe amapeza pa khonsolo kuti khonsolo idzitha kupeza ndalama zoti ingapitirize ntchito zachitukuko patsogolo.

5.3 Thumbali landalama zachitukuko cha m'maboma ang'ono

Ndalama zomwe zimaperekedwa ku maboma a ng'ono zachitukuko zimakhala ndi ndondomeko zake. Thumbali limayendetsedwa ndi gulu loyanganila chitukuko cha m'maboma ang'ono lomwe lili pasi pa Unduna wa Zachuma.

5.4 Ndalama za anthu achifundo ndi mabungwe osakhala aboma

Awa amathandiza ma khonsolo ndi ndalama zapadera zomwe zimathandiza ma pulogalamu komanso ma pulojekiti omwe bungwelo lagwirizana nawo.

6.0 NJIRA ZOYENERA KUTSATA POPANGA KALONDOLONDO WA CHUMA CHA BOMA

CHOYAMBA: Kudziwa komwe kumachokera mfundo zokhudzana ndi kalondolondo wa kagwiritsidwe ntchito kandalama.

Kalondolondo wa chuma cha boma ndiwoyenera kuchitika pafupi-pafupi nthawi zonse. Komanso pamafunikira kukhala wodziwa za mabajeti onse omwe avomerezeka ndi khonsolo, ma pulani a m'maboma, mapulani a m'midzi, malamulo a pa mwezi kapena apanthawi omwe aperekedwa, ma ripoti apa mwezi kapena apakanthawi. Ndikofunika kuti amkhala pampando ndi ena onse ogwira ntchito kukhonsolo awonetsetse kuti makhansala akudziwabwino zonse zokhudzana ndi khonsolo ndiposo ma ripoti onse akufotokoza bwino momveka bwinonso.

Ndime 42 ya malamulo am'maboma ang'ono imafotokoza za ufulu wa anthu onse kudziwa za kayendetsedwe ka zachuma cha m'maboma ang'ono. Kupeza nkhani ndi vuto lomwe lilipo mumaboma ang'ono. Ofesi ya abwana mkubwa ndi maofesi ena otsogolera m'zigawo ndi komwe anthu angathe kupeza nkhani zomwe akufuna kudziwa. M'maboma ang'ono momwe muli vuto lalikulu ndikofunika kuti makhansala atengeko gawo lalikulu kupereka choonadi kudzera mwa otsogolera khonsolo komanso pogwira ntchito limodzi mogwirizana ndi anthu ena ogwira ntchito m'boma ndi ma bungwe ena omwe siaboma kuti amve zoonadi. Makalata ena omwe amapezeka ndi nkhani zofunikira za bajeti ndi momwe maboma ang'ono amagwiritsira ntchito ndalama omwe ma khansala onse amayenera kuwadiwa ndi monga:

Tebulo 2: Komwe tingapeze zofunika kudziwa pa ntchito yopanga kawuniwuni wa chuma cha boma

Buku	Zam'kati mwake	Komwe bukuli limapezeka
Ma bajeti a khonsolo	Ndalama zomwe khonsolo ikuyembekezera kupanga ndi ndalama zomwe Khonsolo itagwiritsire ntchito mu sector iliyonse mchaka chimenecho.	kwa DC ndi Mkulu wa zachuma
Ma pulani a chitukuko cha boma	Ntchito zomwe khonsolo ikufuna kupanga	kwa DC ndi Mkulu wa za maplani a zachitukuko
Ma pulani a chitukuko cha pa chaka	ntchito zofunikira koposa zina zonse zomwe khonsolo ikufuna igwire mchaka chimenecho.	kwa DC/Mkulu wa zachitukuko
Ma pulani a chitukuko cha m'midzi ndi zigawo za boma	Ntchito zomwe zitagwiridwe mumadera osiyanasiyana munthawi yoperekedwayo.	kwa Mkulu wa zachitukuko, ndi akulu akulu a nthambi za boma
Ma lipoti a zachuma apa mwezi ndi pa chaka	ndondomeko ya momwe ndalama zotolerredwa ndi kugwiritsidwa ntchito pa miyezi ndi pachaka chilichonse.	kwa DC, Mkulu wa zachuma ndi komiti yowona zachuma
Malisiti	ma lisiti osonyeza ndalama zomwe khonsolo yakhala ikulandira.	kwa DC, Mkulu wa zachuma
Mfundo zomwe khonsolo yamanga	Mfundo zonse zomwe khonsolo yagwirizana mmisonkhano yake.	kwa DC, Mkulu wa zachitukuko



ZOYENERA KUDZIWA:

Ngati pali vuto lopezera nkhani ndikwabwino kuti ma khansala atengepo gawo ndikugwira ntchito ndi anthu ena ngati a phungu anyumba yamalamulo, ogwira ntchito m'boma ndi mabungwe omwe siaboma kuti apeze nkhani yomwe akufunayo.

CHACHIWIRI:***Kafukufuku wa anthu ogwira nawo ntchito***

Cholinga cha kalondolondo wakagwiritsidwe ntchito ka ndalama za boma ndi kuthandiza ma Khansala, ogwira ntchito pa khonsolo, ena apa khonsolopo, ma CSOs ndi mzika kuti akhale ndi kumvetsetsana pa zomwe amafuna pamoyo wawo wa tsiku ndi tsiku zomwe ndalama zaboma zitha kuwathandiza komanso kuvomereza momwe bajeti yayendera kuti zithu zomwe zakonzedwa zilandiridwe bwino. Motero anthu onse okhudzidwa ayenera kutenga gawo panthawi zonse poti izi zimachitira umboni komanso zimapangitsa kuti anthu amvetsetse momwe ndalama zagwiritsidwira ntchito. Ndikofunikanso kuyankhula ndi anthu omwe akuyimirira anthu ena ndi onse osangalatsidwa kudziwa za kalondolondo wa ndalama zabomayu kuti adziwe ubwino wake. Ndikofunikanso kudziwa anthu omwe ndiokhudzidwa ndikupanga nawo misonkhano ndi anthu ena apa khonsolo, ogwira ntchito pa khonsolo, amabungwe omwe siaboma ndi mzika zomwe ndizokonzeka kutenga nawo gawo pa nkhani zachitukuko cha m'maboma ang'ono. Muganizire magulu atatu ndikuona momwe mungagwirire nawo ntchito limodzi:

- **Abale osangalatsidwa kugwira nawo ntchito:** Magulu onse kapena anthu omwe ali ndi chidwi ndi kalondolondo wakagwiritsidwe ntchito ka ndalama za boma monga ADCs, Atsogoleli amabisinezi, CSOs, atsogoleri, makhansala, andale, aphungu akunyumba yamalamulo, ndi ena otero.
- **Anthu Omwe ali mfundo zenizeni:** Awa ndi anthu ofunikira kwambiri kuti ntchito ya PET iyende bwino.
- **Apangiri:** Magulu/ anthu, mabungwe oyimilira omwe angapititse patsogolo anthu opanga ziganizo kapena anthu omwe angagwire maganizo otsutsana.

**Ntchito yoyamba:**

Pakhonsolo yanu kapena pakomiti ya pa sekishoni komwe mukugwira ntchito, onani ndikulemba mayina aanthu omwe ali m'magulu atatuwa:

- Abale osangalatsidwa kugwira nawo ntchito,**
- Adziwitsi,**
- Opititsa patsogolo kapena kubwezeretsa mbuyo.**

Konzani njira agwiritsidwe ntchito momwe mungagwirire ntchito, kugwiritsa ntchito kapena kugwirira limodzi ndi anthu amenewa kuti mukonze nyengo yabwino yakalondolondo yakagwiritsidwe ntchito kandalama zaboma.

CHACHITATU: Kumvetsetsa momwe maboma ang'ono amalongsolera ntchito za khonsolo, sekishoni ndi Wadi

Ku Malawi khonsolo ya ma boma ang'ono imalemba ma pulani a chitukuko (District Development Plan, DDP) pakatha zaka zisanu zilizonse monga momwe anenera a Malamulo amaboma ang'ono ndi malamulo a chitukuko (Development Planning System Handbook (2011)). Malamulo a DDP amalembedwa molingana ndi VAP ndipo mumalembedwa zonse zofunika pa chitukuko cha mdera (zolembedwa mwandondomeko) zoti zikwaniritsidwe panthawiyo. Chiganizo chachitukuko chilichonse chimakonzedwa moganizira mapulogalamu ndi ma pulojekiti omwe akonzedwa kuti athandizire ntchito zachitukuko. M'madera, atsogoleri, a mabungwe omwe siaboama ndi ena oyang'anira zachitukuko ayenera kutsatira ndondomekozi kuti apeze ma pulojekiti komaso ndondomeko zoyenera zachitukuko.

Bokosi I: Chitsanzo cha zomwe zimapezeka mu DDP

Mfundo zazikulu: Pulani ya chitukuko cha boma la Ntcheu yazaka 2010 -2013 ikusonyeza kuti khonsolo itakambirana idagwirizana kuti ntchito zisanu zoyenera kuti zigwiridwe nsanga zinali izi: 1) kuthetsa njala mmakomo, 2) kubweretsa madzi abwino kwa anthu, 3) kukweza ntchito ya zaumoyo, 4) kuchepetsa kufala kwa matenda a edzi, 5) kuchepetsa umbuli.

Pulogalamu ndi pulojekiti imatambasulidwa monga mwachitsanzo:

Cholinga: Kukweza ntchito ya zaumoyo:

Dzina la chitukuko	Zomwe itapange	Atadyerere ndani	Dera	Nthawi yogwilila ntchito	Ndalama zake	Otsogolela
Kumanga zipatala zazing'ono ndi za azimayi oyembekezera	Kumanga zipatala	a n t h u amuderalo ndi ena	ADCs	2010-2013	33,000,00	Mkulu wa za umoyo
Kugula zipangizo ndi mankhwala	kugula zipangizo ndi mankhwala	anthu amuderalo ndi ena	ADCs	2010-2013		Mkulu wa za umoyo
Kuthetsa khalidwe lakuba mankhwala	Kuthetsa khalidwe lakuba mankhwala	anthu amuderalo ndi ena	ADCs	2010-2013		Mkulu wa za umoyo
Kuchepetsa imfa zauchembere ndi nthumbidwa	imfa za ntchembere ndi nthumbidwa zachepetsedwa	anthu amuderalo ndi ena	ADCs	2010-2013		Mkulu wa za umoyo

Kuchekera ku: Ntcheu District Development Plan (2010-2013)

Molingana ndi ma pulani a pa boma (DDP), palinso ma pulani a mmudzi (VAP) ndi ma pulani a m'masekishoni monga Mapulani a pa boma okhudzana ndi maphunziro (DESP). Mapulani a m'midzi (VAP) amaonetseratu zofunika za m'madera zomwe zimadziwitsa a DDP. Mapulani a munthambi za boma amaonetsera zofunika za pa mthambiyu molingana ndi DDP ndi pulojekiti zomwe zingafunike kuti mapulaniwo akwaniritsidwe. Ma pulani a sekishoni amakhala molingana ndi mapulani a DDP.

Ndikofunika kuti ma Khansala adziwe zofunikira M'maboma ang'ono zomwe zalembedwa mu mapulani a DDP ndi zina zonse zomwe zakonzedwa zokhudzana ndi chitukuko cha m'madera zomwe zalembedwa mu VAP. Kuphatikizira pakudziwa za mapulani, ma Khansala ayenera kudziwanso

njira zomwe zingatengedwe kuti mapulaniwo akwaniritsidwe ndi mabajeti ake onse. Ma membala am'makomiti osankhidwa akhaleso odziwa bwino ma pulani a m'masekishoni ndi momwe zikulunganirana ndi bajeti. Powunika bajeti ya khonsolo ndizina zofunikira za pa boma molingana ndi ma pulani a DDP,VAP, ndi mapulani a sekishoni, makhansala ayenera kudziwitsidwa bwino kuti ma pulaniwo ali ndi bajeti kapena ayi.

CHACHINAYI:

Kumvetsetsa ma bajeti a m'maboma ang'ono

Tebulo 3: Momwe bajeti yapachaka imayendera

Kalendala ya bajeti ya pa chaka M'maboma ang'ono	
Nthawi	Ntchito
Julaye - Okotobala	Kulemba lipoti lomaliza la ndondomeko yam'mene ndalama zayendera
Novembala – Disembala	a National Audit Office amapanga kalondolondo wa ndalama zonse
Novembala – Disembala	kukambirana ndi anthu am'midzi za zomwe akufuna mchaka chikubweracho. (Annual Investment Plan (AIP) and Local Development Plans (LDP)
Disembala	Boma limatulutsa milingo ya mabajeti ndi ndondomeko zake.
Januwale	kukambirana ndi anthu am'midzi za momwe ndalama za (Annual Investment Plan (AIP) and Local Development Plans (LDP) zaperekedwera.
	kupanga ma bajeti
Febuluwale	kukambirana ndi kumalizitsa mabajeti
Malichi	makhonsolo kuvomereza mabajeti
Epulo - Meyi	kuwunika mabajeti onse amaboma ang'ono ndi a National Local Government Finance Committee (NLGFC)
Juni	kupereka mabajeti onse Kunyumba ya Malamulo

a) Kodi bajeti yamaboma ang'ono ndi chani?

Bajeti ya maboma ang'ono ndi pulani yovomerezeka yakapezedwe ka ndalama ndi kagwiritsidwe ntchito ka ndalama kwa nthawi yomwe yapatsidwa monga miyezi 12. Imaonetsa komwe kumachokera ndalama ndi momwe zigwirire ntchito mu ma dipatimenti onse a boma.

b) Mitundu yakagwiritsidwe ntchito kandalama m'maboma

Pali mbali ziwiri zomwe a maboma ang'ono amagwiritsira ntchito ndalama mwakabwereza-bwereza ndi ndalama zachitukuko zomwe zimapezeka mu bajeti yakabwereza ndi mu bajeti ya chitukuko.

c) Bajeti yakabwereza-bwereza:

Bajeti yakabwereza-bwereza imatanthauza ndalama zomwe a khonsolo amazipeza kuchokera ku madera osiyana tsiku lililonse monga malipilo a anthu ogwira ntchito, kulipira ma bilu a magetsi, kulipira maulendo, madzi, misonkhano ndi zina zotero.

d) Bajeti ya ntchito za chitukuko:

Bajeti ya ntchito za chitukuko imasonyeza komwe ndalama za chitukuko zachokera komanso momwe zitagwirire ntchito yake. Nthawi zambiri izi zimayenera kutsatira ntchito zomwe zili zofunikira kwambiri komanso zitukuko zomwe ali mu ma pulani a ntchito za chitukuko pa boma ndi ma pulani a nthambi zachitukuko. Mu bajeti ya chaka cha 2015 mpaka 2016, mwachoka ndalama zina za chitukuko zomwe zapita ku ma khonsolo ngakhale kuti kayendetsedwe ka bajeti yikanaperekedwe ku ma khonsolo mwathunthu. Ntchito zambiri za chitukuko zikuyendetsedwa kuchokera ku likulu la boma ndipo ntchito zina za chitukuko mu maboma ambiri zikupangidwa ndi mabungwe omwe si a boma komanso mabungwe omwe amapereka thandizo la chuma. Izi zikowonetsera poyera chifukwa chomwe kukwaniritsa mfundo zofunikira mu mapulani a chitukuko mu maboma kunali kovuta kwa zaka zambiri. Ngakhale zili choncho, nkofunikira kuti ma khonsolo mogwirizana ndi nthambi zina akambepo pa nkhani yopatsidwa mphamvu potenga nawo gawo pa kayendetsedwe ka bajeti ya chitukuko komanso za malamulo omwe angawonetsetse kuti mabungwe omwe si aboma, mabungwe omwe amapereka thandizo la chuma komanso mabungwe ena akugwira mothathandiza ma khonsolo kukwaniritsa ntchito zomwe zili kale mu mapulani a mu ma boma komanso mapulani a m'midzi ya m'mabomamo.

Makhonsolo m'Malawi ali ndi zikalata zitatu zokhuza bajeti zomwe zimafotokoza kagwilitsidwe ka ndalama polipila zinthu zomwe zimalipidwa pa nyengo ngati malipiro a pamwezi kupatulapo kugula katundu komanso momwe ndalama ya chitukuko ingagwilire ntchito motere: i) Tsatanetsatane wa mabajeti omwe amawonetsa kagwiritsidwe ntchito, kalipidwe ka zinthu zomwe zimalipidwa panyengo koma mowilikiza mwachitsanzo malipilo a pa mwezi ndi ntchito zina kupatula kugula katundu, ii) Mabajeti ongofotokoza zinthu zomwe zikuyenela kukwaniritsidwa mu chaka cha boma komanso bajeti yomwe ili ndi mfundo za momwe ntchito za chitukuko zomwe zitachitike komanso katundu woti agulidwe mu nyengo yomwe yapatsidwa.

Kumvesetsa za ndalama zomwe zimaperekedwa potengera zinthu zomwe zitakwanilitsidwe

Chiyambi cha kulondoloza kagwiritsidwe ntchito ka ndalama za boma ndi kudziwa kaye ndalama zomwe zaperekedwa kuti zigwire ntchito. Bajeti yomwe imakonzedwa malingana ndi zinthu zomwe zitakwaniritsidwe ndiyofunika popereka tsatanetsatane wa zinthu zoti zikwaniritsidwe ndi nthambi zosiyanasiyana za boma. Bajeti yimafotokoza masomphenya, cholinga komanso ndondomeko yomwe itatsatidwe pokwaniritsa cholinga cha khonsolo iliyonse, imasonyezanso zinthu zomwe zinakwaniritsidwa mu chaka chammbuyo, ntchito zina zofunikira komanso momwe ndalama zagawidwira ku nthambi iliyonse komanso zinthu zomwe zakonzedwa kuti zikwaniritsidwe pa chaka ndi nthambi zosiyanasiyana. Mu bajeti yimafotokoza amayenera kuwonetsa zinthu ziwiri izi: Ndalama zomwe zitalandiridwe ndi nthambi zosiyanasiyana komanso zinthu zomwe zakonzedwa kuti zikwaniritsidwa ndi mulingo wake.

**MFUNDO:**

Chiyambi cha kulondoloza kagwiritsidwe ntchito ka ndalama za boma ndi kudziwa kaye ndalama zomwe zaperekedwa kuti zigwire ntchito ku nthambi zosiyanasiyana mu chaka cha bajeti.

M'munsimu muli chitsanzo cha ndalama zoperekedwa ku nthambi zosiyanasiyana mu chaka cha bajeti pofuna kuwonesa momwe bajeti yopangidwa potengera zinthu zomwe zitakwaniritsidwe zimalembedwera. Kudzela mukalembedwe aka, munthu ngati khansala kapena membala wa komiti yoyendetsa ntchito atha kupezamo zoyenera kudziwa zokhudzana ndi zinthu zomwe zaperekedwa kapena kulembedwa mu bajeti ya nthambi yomwe akugwirako ntchito.

Tebulo 4: Chitsanzo chandalama zomwe ma sekishoni ena anapeza (2012/13)

Nthambi	ndalama zomwe zidaperekedwa 2011/12	Zomwe zidagwiritsidwa ntchito 2011/12	zomwe zidali pa ndondomeko	kukwera kapena kutsika wake
2012/13	19,491,404	19,491,404	19,491,404	0
Maphunziro	86,875,132	169,445,132	216,438,235	149
ZaUmoyo	457,923,008	428,272,925	415,446,363	-9
Madzi	962,056	962,056	962,056	0
Zoti pasakhale kusiyana palatial pa abambo ndi amayi	5,036,678	5,036,678	5,036,678	0

Ngakhale zili choncho, kulumikizitsa ndalama zomwe zitagwirire ntchito, makhonsolo ayenera kudziwa zinthu zomwe anakonza kuti akwaniritsa komanso mulingo womwe anakhazikitsa kuti akwaniritsa wa nthambi iliyonse ya khonsolo. Bajeti ya imafotokozanso za ma pulogalamu ena ang'onoang'ono, zinthu zoti zikwaniritsidwe ndi mulingo womwe tikufuna kukwaniritsa.

Tebulo 5 Chitsanzo chamomwe amapangira chionetsero chazomwe apanga kuchokera ku Sekishoni ya Ulimi

Tebulo 5: Mapulani a pachaka ndi apa nyengo kuchokera ku nthambi ya zaulimi

Chigawo	Chigawo cha chin'gono	Zofuna kupanga	Annual Target	Q1 Target	Q2 Target	Q3 Target	Q4 Target
Ulimi	Ntchito ya ulimi wa mbeu	Malo amene akupangidwa ulimi wa makono	75834	0	17278	47282	11274
		Mkhokwe zazin'gono zikugwira ntchito	10	0	5	0	5
		Mitengo ya zipaso yazalidwa	260	0	160	100	
	Ntchito Zosamalira nthaka	Malo amene kukupangidwa ulimi wosamalira nthaka	13600	5533	3000	0	5067
	Ulangizi	Alimi amene afikiridwa ndi ulangizi	189588	0	43196	118206	28186
	Ulimi wa bizinezi	Alimi amene alumikizidwa ku misika	5	2	1	0	2
		Alimi amene aphunzitsidwa agro-processing	1000	300	300	0	400



Chochita chachiwiri:

Tangani bajeti yofotokoza zinthu zomwe zikuyenela kukwaniritsidwa ndi khonsolo yanu. Pogwiritsa chitsanzo mu table 4, pezani ntchito zomwe zikuyenera kukwaniritsidwa komanso mulingo womwe munakhazikitsa kuti mukwaniritsa pa chaka komanso mu miyezi inayi iliyonse ya pa chaka ya nthambi ya komiti yomwe inuyo ndi membala. Zomwe mwapeza zikuyimira zochitika zomwe zakonzedwa kuti zikwanilitsidwa ndi nthambi yanu ndi ndalama zomwe zakhazikitsidwa kuti ziperekedwa. Tinganenenso kuti zomwe zili mu bajeti ziyenera kugwiritsidwa ntchito pokwaniritsa ntchito zomwe zinakonzedwa. Fanizani zomwe zinakhazikitsidwa kuti zikwaniritsidwa ndi ntchito zomwe munayika kuti ndizofunika kwambiri mu ma pulani achitukuko ndi momwe ndalama zikugwiritsidwira ntchito.

Kuwerenga komanso kumvetsa tsatanesatane wa ndalama zongoyerekeza zogwilira ntchito mu bajeti.

Bajeti yokonzedwa poyerekeza ndalama zomwe zingafunike ndiyofunika polondoloza momwe ndalama zikugwiritsidwira ntchito chifukwa imagwiritsidwa ntchito ndi anthu owona komanso kuwerengera ndalama pokonza ndondomeko zoyendetsera ndalama. Imathandizanso kayendetsedwe ka ndalama polinganiza ndalama zomwe zagwilitsidwa ntchito ndi zomwe zinakonzedwa mu bajeti kuti zidzagwiritsidwa ntchito. Zimathandizanso ma khansala kudziwa ndalama zolowa komanso zotuluka mu ma pulogilamu a nthambi zawo. Tebulo 6 ikufotokoza za ndalama zomwe zimalandiridwa pa nthawi pa nthawi zoperekedwa ku ma pulogilamu ang'ono ang'ono omwe ali pansu pa ma pulogalamu ena pogwiritsa ntchito chitsanzo cha nthambi ya ulimi.

Tebulo 6: Ndalama zoperekedwa za bajeti ku nthambi ya Zaulimi

Gawo	ORT
Ulimi wa mbeu	5,763,500
Kusamalila nthaka	3,600,223
Ulangizi	10,500,256
Mfundo zopititsa patsogolo ulimi wa bizinesi	6,756,400

Zonse zomwe zalembedwazi zili pa nthambi zonse chikalata chofotokoza tsatane tsatane wa muyezo wongoyelekeza wa ndalama omwe utha kugwiritsidwa ntchito.

Table 6: Chitsanzo kuchokera ku ndalama ndi ma pulani achitukuko

No	Chitukuko	Dera	Gawo	kuyamba	Kumaliza	Zopangidwa	Zizindikiro za pulojekiti	zofunika mu pulojekiti	Bajeti yo vomerezedwa	Kochokera ndalama
1	Ntchito zazing'ono za CDF	Ma konsitichuwense onse	Kosiyana siyana	Jul-15	Jun-16	Zitukuko zazing'ono za CDF zapangidwa	Nambala ya zitukuko zapangidwa	Zizadziwikabe	60,000,000.00	CDF
2	Kukonza zimbuzi zam'misika	Ofesi ya boma ndi msika, mnthalire	Kulikulu	Jul-15	May 16	Nambala ya zimbuzi zimene zakonzedwa	Nambala ya zimbuzi zimene zakonzedwa	Zosiyana siyana	7,738,380.00	Ndalama zimene khonsolo imapeza yokha
3	Kugula ma kompyuta	Ofesi ya DEM	Maphunziro	Sept-15	Oct-16	Ma kompyuta agulidwa	Nambala ya ma computer agulidwa	2	1,149,250.00	ORT
4	Kumanga Nyumba za anthu osamalila odwala pa Makhwira Health Centre	Ofesi ya M'kulu wa za umoyo	Umoyo	Aug-15	April-16	Nyumba za anthu osamalila odwala	Nambala ya nyumba za anthu osamalila odwala zomwe zamangidwa	1		Bajeti ya chitukuko

CHACHISANU: Kulondoloza ndalama za boma

Tikapeza zofunikira mu bajeti, nkotheke kuyamba kuwona momwe ndalama zagwiritsidwira ntchito pofananiza ndi ndalama zomwe zinakhazikitsidwa kuti zigwire ntchito mu bajeti pa mwezi uliwonse. Nkofunika kuyamba kuwunika nthambi iliyonse payokha monga ya za umoyo, maphunziro, ulimi ndi madzi. Makhansala ndi anthu kapena mabungwe othandiza ntchito za boma atha kukambirana kuti ayambe nthambi iti.

Gawo loyamba:

Choyamba kuchita ndi kuwonkhetsa ndalama zomwe ziyikidwa kuti ziperekedwa ku nthambi zosiyana mu bajeti ya khonsolo, ndikufananiza ndi ndalama zenizeni zomwe zinalandiridwa ndi khonsolo kuchokela madera osiyanasiyana ndi ndalama zomwe zinagwiritsidwa ntchito ndi nthambi iliyonse mwezi ndi mwezi. Zinthu zonse zotithandiza kuti tiwerengere bwino zikuyenera kuchokera mbali zosiyanasiyana kuti pakhale chikhulupiliro cha zomwe tapeza. Izi zizathandiza ma khansala komanso anthu omwe ali mu makomiti a Zantchito kudziwa kuti ndi ndalama zingati mwa ndalama zomwe ziyikidwa mu bajeti kuti zilandiridwa, zikulandiridwadi ndipo ndikudziwanso kuti zingati zomwe zikugwiritsidwa ntchito ndi nthambi iliyonse. Kukwaniritsa zochitika zomwe zinakonzedwa zimatengera kupezeka kwa ndalama ndi zinthu zina zomwe zili mu bajeti ndi kagwiritsidwe ntchito ka zinthu za mu bajeti zomwe zapezeka ku zochitika zomwe zinakonzedwa kuti zichitike.

Gwilitsani tebulo 7 kuti mulembe mfundo za zomwe mwapeza

Tebulo 7: Kupanga kawuni wuni

Kufanizira ndalama zomwe zinayikidwa pa Bajeti ndi zomwe Khonsolo inalandila ndi kugwiritsidwa ntchito mu sekita iliyonse.

Gawo	Ndalama za pa bajeti	Zomwe zalandiridwa mwezi uliwonse	Zomwe zagwira ntchito pa mwezi uliwonse	Ndalama zotsalira
ZaUmoyo				
ZaMaphunziro				
Zaulimi				
ZaMadzi				

* Ngati pali ndalama zotsala, fufuzani kuti zatsala chifukwa chani komanso ndalama zotsalazo zigwira ntchito yanji.

Gawo lachiwiri:

Chachiwiri ndi kuwunika cholinga chomwe ndalama zinagwiritsidwira ntchito polingalira ntchito zomwe zinakhazikitsidwa kuti zikwaniritsidwe ndi mulingo wake. Nthawi iyi, nkofunika kulemba zonse zomwe mwawona za momwe ndalama zikugwiritsidwira ntchito-kaya mu ma pulogilamu ena ang'onoang'ono, ntchito zomwe zikuyenera kukwaniritsidwa kapenanso zinthu zina ndi zina. Funso lofunika kufunsa ndilakuti: Ngati ndalama ndi zinthu zina zofunikira sizikugwiritsidwa ntchito pa zinthu zomwe zinakonzedwa, zikugwiritsidwa ntchito yotani?

Tabulo 7a: Kalondolondo wa Ndalama 2: *Kufanizira ndalama zomwe zagwiritsidwa ntchito mu sekita iliyonse mwezi uliwonse pa subprogram iliyonse muza Ulimi*

Gawo	Ndalama zomwe zidagwiritsidwa pa gawo pa mwezi	Ntchito zomwe Ndalamazo zagwira	zimene zaoneka mukagwiritsidwe ntchito kandalamazo
Zaulimi wa mbeu			
Kusamala malo			
Ulangizi			
Ulimi odzitsata			

Tabulo 7b: Kalondolondo wa Ndalama 2: *Kufanizira ndalama zomwe zagwiritsidwa ntchito mu sekita iliyonse mwezi uliwonse pa subprogram iliyonse- za Umoyo:*

Gawo	Ndalama zomwe zidagwiritsidwa pa gawo pa mwezi	Ntchito zomwe Ndalamazo zagwira	zimene zaoneka mukagwiritsidwe ntchito kandalamazo
Sukulu za mmera mpoyamba			
Sukulu za pulaimale			
Sukulu za Kwacha			

Tabulo 7c: Kalondolondo wa Ndalama 2: *Kalondolondo wa Ndalama 2: Kufanizira ndalama zomwe zagwiritsidwa ntchito mu sekita iliyonse mwezi uliwonse pa subprogram Zaumoyo*

Gawo	Ndalama zomwe zidagwiritsidwa pa gawo pa mwezi	Ntchito zomwe Ndalamazo zagwira	zimene zaoneka mukagwiritsidwe ntchito kandalamazo
Edzi			
Zamagulu azakudya			
Ziwiya, zipangizo, nyumba ndi zina zofunikira pa zaUmoyo			
ntchito zakupewa matenda			
Ntchito zochiza matenda			
Ntchito zaUkhondo			

Gawo lachitatu:



Gawo la chitatu ndi kuwona zinthu zomwe zakwaniritsidwa pa mulingo womwe unakhazikitsidwa kuti ukwaniritsidwa mu miyezi inayi iliyonse pa chaka. Momwe zafotokozeredwa mu table 4, bajeti yokonzedwa potengela ntchito zomwe zitakwaniritsidwe ikulongosola za mapulogalamu a pansu pa nthambi iliyonse, zinthu zomwe zinakonzedwa kuti zikwaniritsidwa komanso mulingo woyenela kukwanilitsa. Mukawona momwe ndalama zikuyendera, nkofunika kuwona zinthu zomwe zakwaniritsidwa, kapena zomwe zalepheleka mu miyezi inayi iliyonse. Tebulo 8 ikuwonesa momwe kulondoloza zochitika ndi mulingo woti ukwanilitsidwe imalembedwela.

Tebulo 8:

Kuunika ntchito zomwe zagwiridwa mugawo la zaulimi

Chigawo	Chigawo cha chin'gono	Z o f u n a kupanga	Target for the quarter	Actual achievement for the quarter	Major reasons for achievement or under/over achievement
Ulimi	Ntchito ya ulimi wa mbeu	Malo amene akupangidwa ulimi wa makono			
		Mkhokwe zazin'gono zikugwira ntchito			
		M i t e n g o ya zipaso yabzalidwa			
	Ntchito Zosamalira nthaka	Malo amene kukupangidwa ulimi wosamalira nthaka			
	Ulangizi	Alimi amene afikiridwa ndi ulangizi			
	Ulimi wa bizinezi	Alimi amene alumikizidwa ku misika			
		Alimi amene aphunzitsidwa agro-processing			

CHACHISANU NDI CHIMODZI:***Kawuniwuni wa Zotsatila***

Zonse za momwe ntchito ikuyendera zikuyenera kuwunikidwa kuti malipoti omwe amalembedwa pakadutsa miyezi inayi iliyonse alembedwe kuti mabungwe othandiza ntchito za boma athe kuwerenga momwe zikuyendera. Kuwunikaku kumathandiza kuwona malo omwe tikuchita bwino, zofooka kapena mavuto omwe alipo pa kayendetsedwe ka ndalama mu nthambi iliyonse. Zimathandizanso khonsolo kukhazikitsa ndondomeko zopititsa patsogolo momwe ntchito zikuyendera.

- i) Powunika zinthu zomwe zikupezeka mukagwiridwe ka ntchito onetsetsani zinthu izi: Mgwilizano wa zinthu zomwe zinakonzedwa kuti zichitika ndi mapulani a muboma lililonse kapena nthambi ya khonsolo mu bomalo.
- ii) Komwe kukuchokera ndalama za nthambi iliyonse payokha
- iii) Kusiyana kwa ndalama zomwe zili mu bajeti ndi ndalama zenizeni zomwe zikuperekedwa ku nthambi iliyonse ya khonsolo pa mwezi.
- iv) Kodi ndalama zolandira zikugwira ntchito yake?
 - a. Kodi pali ndalama zotsala pa mwezi? Nanga ndalama zotsala zikugwiritsidwa motani?
 - b. Kodi nthambi iliyonse ikugwiritsa ntchito ndalama motani? Kodi ndalamazo zikugwiradi ntchito yake momwe zinalembedwera mu bajeti?
 - c. Ngati ndalamazo sizikugwira ntchito yake, zikugwila ntchito yotani? Ndi chani chomwe chikupangitsa kuti ndalamazi zigwire ntchito motere?
- v) Kodi mulingo womwe unakhazikitsidwa kuti ukwaniritsidwa ukukwaniritsidwadi? Chifukwa chiyani?
- vi) Ndi ndondomeko ziti zomwe zakhazikitsidwa pothana ndi mavuto omwe alipo?

CHICHISANU NDI ZIWIRI***Kufalitsa Mauthenga***

Lipoti ya momwe ndalama za boma zayendera ndi chinthu chofunika pokhazikitsa chikhulupiliro ndi kuchotsa nkhawa ndi chinyengo. Kutu izi zitheke timadalira ma khansala kukhala ndi luntha lolongosola ndi kupereka uthenga mu njira yophweka komanso yosavuta kumvetsa. Lipotili lithanso kugwiritsidwa ntchito kupempha zinthu zina ku likulu la maboma. Nkofunika kuperekanso lipotili kwa mabungwe kapena anthu omwe angathe kuchitapo kanthu pa zomwe zili mu lipotili. Likuyenelanso kukambidwa ku khonsolo pa misonkhano yomwe imachitika pakatha miyezi inayi iliyonse kuwunika momwe akuluakulu angayankhire mfundo zomwe zili mu lipotili.

Ngati kuli kofunika, pulani ikuyenera kukhazikitsidwa pa mavuto onse omwe apezeka. Lipotili likuyenera kugwiritsidwa ntchito pokopa anthu omwe ali ndi chidwi ndi pulojekiti ndi ntchito za maboma ang'onoang'ono. Ma lipoti ena a pa boma atha kugawidwanso ku ma ofesi akulu akulu monga National Local Government Finance Committee komanso nthambi ndi mabungwe ena omwe amayang'anira makhonsolo.

7.0 Zinthu zomwe zingapangitse kuti Kalondolondo wa Ndalama zam'Maboma ang'ono ayende bwino ndi:

Kugwirira ntchito limodzi

Kugwira ntchito limodzi nkofunika. Pa Chichewa amati 'Mutu Umodzi susenza denga', 'Kukhala awiri simantha', nkofunika kuti makhansala adziwe ndi kumvetsetsa mphamvu zomwe mabungwe ena othandiza boma ali nazo kuti athe kukonza njira zogwirira ntchito limodzi kuti akwaniritse kulondoloza kagwiritsidwe ntchito ka ndalama. Nkofunikanso kulimbikitsa kugwira ntchito limodzi ndi nthambi zina za boma, maunduna komanso magawo ena chifukwa zotsatira za kulondoloza momwe ndalama za boma zayendera kumapangitsa kuti ndondomeko zina za kayendetsedwe ka chuma zisinthe kupangitsa kulondoloza kwa ndalamaku kukhala kofunikira kwa mbadwa za dziko.

Kulondoloza kosalekeza

Kulondoloza ndalama za boma kusakhale ntchito yongopanga kamodzi nkusiya. Kuti zinthu zisinthe, kulondoloza momwe ndalama zayendera kukuyenera kukhala kosalekeza komanso kukhala ngati gawo la ntchito komiti yoyendetsa ntchito za khonsolo.

Kwina komwe mungathe kupitiliza kuwerenga za malangizowa ndi uku:



- Malawi Local Government Association (2014). A Handbook for Councillors and other Council Members. Lilongwe, MALGA
- International Budget Partnership: www.internationalbudget.org: The International Budget Partnership collaborates with civil society around the world to use budget analysis and advocacy as a tool to improve effective governance and reduce poverty.
- National Democratic Institute (NDI) political process monitoring guide: https://www.ndi.org/political-process_monitoring_guide : This guide was developed to primarily explore the work that the Institute and its partner groups have conducted across five types of political-process monitoring , legislative monitoring; budget monitoring, budget advocacy and expenditure tracking; shadow reporting; monitoring government follow-through; and election campaign-related monitoring.
- National Democratic Institute (2010). Supporting Local Governance in Yemen. Steps to Improving Relationships between Citizens and Government: Manual for Local Councillors, Civil Society Organizations and Citizens
- Narayan, D. (2002). Empowerment and poverty reduction: A sourcebook, Washington, DC: The World Bank.



National Democratic Institute ndi bungwe lothandiza mwachifundo, losayimira chipani chilichonse komanso silaboma, limene limakhudzidwa ndi zikhumbokhumbo za anthu padziko lonse lapansi kuti akhale muufulu ndi kulimbikitsidwa pa nkhani ya ufulu wachibadwidwe.

Off Mwambo Road, Plot 12/332
P.O. Box 41,
Lilongwe, Malawi

www.ndi.org